

# ZINSINSI ZA PAPA

Olemba Tony Alamo  
*inalembedwa m'chaka cha 1983*

Vatican ikudzionetsa ngati kuti iyoyo ndi oyera ngati Chipale, koma Baibulo limasonyeza kuti ndi hule, kapena kuti, “**mkazi wachigololo wamkulu**,” waupandu (Chivumbulutso 19:2).<sup>1</sup> Tchalitchichi chimagwiritsa ntchito nthambi za boma m'mayiko onse, kuphatikizapo la United States, ngati atumiki ake ankhanza kwambiri. Tchalitchichi chikakhala ndi mphamvu zambiri m'boma ndipamene chingamadzibise podzionetsa ngati kuti icho “ndichoyerwa ngati Chipale” ndicholinga choti boma lizinenedwa komanso kuukiridwa chifukwa cha zoipa zimene tchalitchi chikuchita kuseri kwa boma.

**CHOLINGA:** Kuika malamulo ozunza, opondereza, owononga, ndiponso othana ndi aliyense komanso maganizo osiyana ndi a Roma Katolika n'cholina choti tchalitchichi chikhale monga mfumukazi ya Satana (mkazi wachigololo wamkulu).

Chifukwa chofunitsitsa kuyendetza boma la dziko lapansi ndi tchalitchi, Vatican yomwe ili ngati njoka yawononga dziko lapansi komanso boma la United States ndi zambiri za khama lake, kuphunzitsidwa mwaukadaulo ndi kutsatira Yesuit modziperekwa, mwakuti panopa tchalitchichi chikulamulira United Nations (imene chinayambitsa),<sup>2</sup> Nyumba ya Chifumu ku U.S., chipani cha Congress, chigawo chili-chonse m'dzikoli, chitaganja, mzika, ndi magulu a mabungwe a boma, kuphatikizapo Dipatimenti Yoona za Ntchito ku U.S., bungwe la IRS, FBI, Khoti Lalikulu, makhoti onse, asilikali ankhondo, zigawo, apolisi, chitaganja, ndi ena a polisi, komanso mabanki akuluakulu padziko lonse ndiponso banki zazikulu m'dzikola U.S. (zotchedwa Illuminati ndi Agentur), mabungwe oona za anthu a pantchito,<sup>3</sup> gulu la Mafia, ndiponso nyumba zikuluzikulu zofalitsa nkhanzi.

Chipembedzo chimenechi (Cha Vatican) changotsala pang'ono kusintha dzina la malamulo oyendetsera dziko lathu la U.S. ndi dziko lake limodzi, malamulo ake akupha ausatana kukhala “chikunja” (munthu aliyense amene si wa Roma Katolika). General Lafayette, Mkulu wa asilikali olemekezedwa kwambiri olondera Pulezidenti George Washington, ananena mwafulosi kuti, “**Ngati ufulu wa anthu a dziko la Amerika ungasokonezeke, udzasokonezedwa chifukwa cha akuluakulu a chipembedzo cha Roma Katolika.**”<sup>4</sup>

Lero tikuona nkhanzi zitafika paindeinde zimene zinalankhulidwa ku Australia ndi Bishopu Wamkulu wa Roma Katolika, dzina lake Gilroy papufupi zaka 50 zapitazo. Awa ndi ena mwa mawu amene iye ananena:

“**A Roma Katolika amayendera mfundu yakuti tizigwirizana Akatolika tokhatokha basi. Tikamaponya mavoti, tigon-jetse anthu onse achikunja [omwe si a Roma Katolika]. Abambo oyera amati kuchita zinthu zosiyana ndi mfundu imeneyi n'koopsa. Zimene abambo oyera akufuna [papa] n'zakuti posachedwapa akuluakulu a boma akhale a Roma Katolika 100%. Izi ndizofunika kusamala kuti anthu asayambe kuyakira pamene maudindo akuluakulu m'boma akuperekeda-wa mwachinsisi kwa anthu ambiri a Roma Katolika kusiyana ndi Mapulotesitanti, Ayuda, ndi anthu ena achikunja.**”



Anthu mamiliyonu ambirimbiaphedwa ndi Vatican, monga mmene Ambuye ananenera (Chivumbulutso 18:24). Ndipo mbiri yonse ya anthu ikusonyeza kuti zimenezi n'zoona. Mwachitsanzo, Tchalitchi cha Roma Katolika chinkazunza kwambiri anthu ku mayiko a ku Ulaya. Pa nthawi imene gulu la mpingo wa Chiroma linkachita kafukufuku wankhanza ku Ulaya anthu 68 miliyoni anazunzidwa, kupundulidwa, ndi kuphedwa ndigululi.<sup>5</sup> Pa tsiku la kufa kwa anthu ambiri mwa nkhanza la St. Bartholomew panaphedwa anthu okwana 100,000 chifukwa choti sanali Akatolika.<sup>6</sup> Pulezidenti Abraham Lincoln anadzudzula udindo wa papa chifukwa choyambitsa nkhondo yapachi-weniwi m'mawu awa:

**“Nkhondo imeneyi sikanayambika n'komwe kupanda anthu achinyengo otchedwa Jesuit omwe ndi akuluakulu a Katolika ku kolezera moto mwanseli. Chifukwa cha mpando wa upapa ndichifukwa chake panopa tikuona dziko lathu lili phyu ndi magazi okhaokha a anthu ake.”** Lincoln anapitiriza kunea kuti, “Ineyo ndikufuna kuti ufulu m'maganizo weneweni uoneke pakati pa anthu. Koma sindingapatse ufulu wamaganizo kwa papa ndi anthu amene amamutsatira, a Roma, bola ngati andiuza, kudzera mwa alangizi awo onse, aphunzitsi, ndi malamulo a chipembedzo chawo kuti ufulu wawo unawalamula kuwotcha mkazi wanga, kunyonga ana anga, ndiponso kudula khosi langa atapeza danga.”<sup>7</sup>

Popeza Abraham Lincoln anaulula zinthu zambiri zimene Vatican inkachita, iye anaphedwadi monga mmene analoserera. Ndithudi, iye anaphedwa ndi maJesuit omwe anatumidwa ndi Rome.<sup>8</sup> Mpaka pano, monga mmene zinalili m'nthawi ya a Lincoln, Vatican sinasinthebe.

## TCHIMO LIMENE LINAPHETSA J.F.K.

Pamene Vatican inafunsa Bambo John F. Kennedy kuti, “Kodi mudzagwirizana ndi malamulo a Roma kapena malamulo oyendetsera dziko la U.S.?” Bambo Kennedy anayankha pakunena kuti, “Malamulo oyendetsera dziko la U.S.”<sup>9</sup> Yankho limeneli linali tchimo lomwe linaphetsa Pulezidenti Kennedy. Rome analamula zoti iye aphedwe, ndipo amene anakonza mapulani omuphera komanso kumupha anali maJesuits, monga mmene anachitiranso ndi Pulezidenti Lincoln. Aliyense amene ankadziwa zambiri zokhudza kuphedwa kwa Bambo Kennedy nayenso ankaphedwa.

Pamene anthu a ku America anafuna zoti nkhanzi ifufuzidwe, Mkulu Woona za Malamulo Earl Warren (membala wa gulu la chinsinsi la Vatican lotchedwa Knights of Columbus) anasankhidwa kuti apange kafukufuku. Iye anayankhula ndipo anachita zinthu zambiri—pofuna kuoneka ngati akufufuza nkhanzi—kenako, patapita nthawi yomuyenereza, anasiya kufufuza nkhanzi. Izi zinagwirizana ndi mawu apapa akuti, “Zinthu zolakwika zimaphetsa.” Tisaiwale kuti Pulezidenti Kennedy ankamusilira komanso anali wophunzira wa Abraham Lincoln ndipo ankadziwa zimene a Lincoln ankadziwa.

<sup>1</sup> Chiv. 17:1-5, 15   <sup>2</sup> Vatican Imperialism in the Twentieth Century, Avro Manhattan, tsa. 167-170   <sup>3</sup> Vatican Imperialism in the Twentieth Century, Avro Manhattan, tsa. 162   <sup>4</sup> 50 Years in the “Church” of Rome, Charles Chiniquy, tsa. 483 (orig. unabridged 1886 version, available as PDF, tsa. 342)   <sup>5</sup> Smokescreens, Jack Chick, tsa. 35   <sup>6</sup> History of the World in a Christian Perspective, Vol. II, A Beka, 1981, tsa. 352   <sup>7</sup> 50 Years in the “Church” of Rome, Charles Chiniquy, tsa. 498, 503 (orig. unabridged 1886 version, available as PDF, tsa. 352, 355)   <sup>8</sup> 50 Years in the “Church” of Rome, Charles Chiniquy, tsa. 512 (orig. unabridged 1886 version, available as PDF, tsa. 361)   <sup>9</sup> Vatican USA, Nino LoBello, Trident Press, tsa. 79, 161-166

Nkhondo Yachiwiri Yapadziko Lonse, yomwe inaphetsa anthu oposa 30 miliyoni (Ayuda 6 miliyon—omwe anaphedwa ndi a chipani cha Nazi),<sup>10</sup> inayambitsidwa komanso kulimbikitsidwa ndi Vatican—Hitler, Mussolini, ndi Franco onsewa anali mamembala a gululi (chipembezo cha Roma Katolika)<sup>11</sup> —ndipo cholinga chawo chiniali choti awine dziko, osati kuti likhale m'manja mwa Kristu, koma mwa Vatican, omwe ndi otsutsana ndi Kristu.

Kusokonekera kumene kunalipo ku Central ndi South America, nkhanza zimene Castro<sup>12</sup> yemwe anaphunzitsidwa ndi Jesuit ankachita ku Cuba ndi ku Caribbean konse, komanso zauchigawenga ku Lebanon ndi ku Ireland lero ndi ntchito zamanja za Vatican. Mukutha kuona tsopano chifukwa chake Mulungu amanena kuti chipembedzo cha Roma Katolika ndi mayi wa zinthu zonse zonyansa padziko lapansi (Chivumbulutso 17:5)?

Nkhondo Yachiwiri Yapadziko Lonse itatha, a Vatican anadziwa zoti anthu ambiri akudziwa zoti Vatican ndi imene inayambitsa nkhondoyo, choncho anaganiza zopeza njira yowaphimbira anthu m'maso, ndipo anayambitsa John Birch Society n'cholinga choti anthu aziganiza komanso kukamba za Chikomyunizimu (chomwenso chinkalimbikitsidwa ndi Vatican) m'malo mwa wolakwitsa weniweniyo (Vatican). Pulani imeneyi inawayenderadi kwambiri.

Vatican ndi imenenso ikuthandiza gulu lililonse lalikulu lauchigawenga padziko lonse lapansi. Cholinga chawo n'choti anthu aziganizira zauchigawengazo pomwe iwovo a Vatican akutan-ganidwa ndi kuyesetsa kuchita zinthu zosonyeza kuti maboma a padziko lonse aoneke kuti sakutha kulamulira, kuti apezerepo mwayi wolamulira dziko lonse lapansi (ulamuliro wa papa). Zauchigawenga zikachitika, zimakhala zomvetsa chisoni kuti ofalitsa nkhanzi amafalitsa kwambiri zimenezi kusiya zoti a ku Vatican akufuna kuchotsa malamulo oyendetsera dziko la U.S., ndizoti anthu akulandidwa ufulu wavo wolambira (akumangidwa, masukulu ndi matchalitchi akutsekedwa). Izi n'zimene a ku Vatican akufuna kwambiri, kuti azilamulira zipembedzo zathu komanso maboma athu padziko lonse lapansi. Iwo akuona kuti zauchigawenga zoipa kwambiri zikamachulukirachulukira, zinthu ziziwayenderanso bwino kwambiri. Nyumba zofalitsa nkhanzi zimene zimagwirizana kwambiri ndi Vatican zikulimbikitsa kufalitsa nkhanzi zauchigawengazi n'cholinga choti inuyo musamaganizire n'komwe zinthu zoipa zimene tchalitchichi chikuchita. Popeza panopa anthu adziwa njira zavo zachinyengo, posachedwa (mogwirizana ndi nyumba zavo zofalitsira nkhanzi komanso pulezidenti wa ku United States, amene walowa m'gululi chaposedchedwapa) ayam-bitsa ntchito yapadera yothana ndi zauchigawenga (zimene anaziyambitsa okha) n'cholinga choti anthu aziwaona kuti iwo ndi ab-wino komanso oopa Mulungu, ndipo sangathandize magulu ochita zoipa. (Chidziwitso: monga Terry Waite kukambirana zodzetza mtendere ku Lebanon.)

Jim Jones, dikoni wagulu la Jesuit la Roma Katolika yemwe anakkala ngati ndi m'hristu, anaperekedwa mseme (osati ndi chakumwa cha poizoni), anaphedwa, pamodzi ndi anthu ena a m'tchalitchi, ndipo amene anawapha ndi a Vatican pofuna kuti anthu padziko lonse azikayikira Akristu a mtima woono.<sup>13</sup>

**"Ziripo zinthu zisanu ndi chimodzi Mulungu azida; inde, zisanu ndi ziwiri zimnyansa: Maso akunyada, lilleme lonama, ndi manja akupha anthu osachimwa; Mtima woganizira ziwembu zoipa, Mapazi akuthamangira mphulupulu mmangu mmangu; Mboni yonama yonong'ona mabodza, Ndi womenyanitsa abale"** (Miyambo 6:16-19).  
**(Akuluakulu a ku Vatican ausatana amachita zinthu zon-sezi zimene Mulungu amadana nazo.)**

Kodi munaona zoti a dipatimenti yoona zolowa ndi zotuluka komanso kutoleka misonko m'dziko la United States, omwe amayendera maganizo a akuluakulu a ku Vatican amanetsetsa kuti munthu asatuluke m'dziko lino popanda kuunikidwa bwinobwino (kufufuz-

idwa, makina owunika munthu, ndi zina zambiri)? Koma m'zaka za m'ma 1960, pamene mkulu waJesuit amene anaphunzira ku Vatican, dzina lake Timothy Leary<sup>14</sup> anayamba kutsogolera achinyamata kuti azigwiritsa ntchito mankhwala osokoneza bongo, zinkaoneka kuti dipatimenti yoona zolowa ndi zotuluka komanso kutoleka misonko, monga mmenenso zilili masiku ano, ikulephera kugwira ndi kulanda mankhwala osokoneza bongo olemera makilogalamu ambirimbiri olowa m'dziko lathu lino limene linali labwino omwe akulowetseda ndi magulu a Mafia, omwenso amasinta ndalamu mwachinyengo ndikupeza phindu mnjira zosayenera (ndalamu zake zonse zachinyengo) mogwirizana ndi a ku Vatican. Mwina izi n'zimene zinachititsa Pulezidenti Abraham Lincoln kunena kuti, "**Ndikuona mtambo wakuda kwambiri ukubwera ku America. Mtambo waku-dawo ukuchokera ku Rome.**"<sup>15</sup>

Taonani zimene Baibulo limanena zokhudza Wokana Kristu zimene zikuyambitsa katangale yenseyu ndikukhetsa magazi onsewa:

**"Ndipo ndinaona mkazi [waku Vatican] woledzera ndi mwazi wa oyera mtima, ndi mwazi wa mboni za Yesu; ndipo ndinadabwa pakumuona iye ndi [kuzizwa] kwaku-kulu"** (Chivumbulutso 17:6).

**"Monga momwe unadzichitira ulemu, nudyer- era, momwemo muuchitire chouzunza ndi chouliritsa maliro: pakuti unena mumtima mwake, Ndikhala ine mfumu, wosati wamasiye ine, wosaona maliro konse ine."** (Chivumbulutso 18:7).

**"Iwo [maboma] ali nawo mtima umodzi, ndipo aper-eka mphamvu ndi ulamuliro wavo kwa chirombo,"** kuanthauza boma limodzi lolamulira dziko lonse, kuphatikizapo mayiko, mabungwe ndi nthambi za boma, ndipo mphamvu zake zikuchokera kwa Satana, ndipo iwo akupereka mphamvuzo kwa okana Kristu kuti achite zofuna zake (Chivumbulutso 17:13).

Izi ndi zina mwa zizindikiro zomaliza zimene zili m'buku la Baibulo la Chivumbulutso zimene zikuoneka Yesu asanabwerenso padziko lapansi ndipo kwangotsala kanthawi kochepa. Mulungu anawononga dziko lonse lapansi ndi madzi,<sup>16</sup> Sodomu ndi Gomora ndi moto ndi sulfure.<sup>17</sup> Pa nthawi zonsezi, Mulungu ankatumiza atumiki ake kudzalengeza za chiwonongeko chimene chikubwera-cho. Masiku anonso, Mulungu chifukwa cha chifundo chake chachikulu, akuchenjeza anthu onse a Roma Katolika kuti, "**Tulukan m'menemo, anthu anga, kuti mungayanjane ndi machimo ake, ndi kuti mungalandireko ya miliri yake**" (Chivumbulutso 18:4). Ngati inuyo muli mmodzi wa anthu a Mulungu, ngati Mzimu wopatsa moyo wakufulumizitsani kuti mulandire moyo wosatha, mukufunika kumvera Mawuwa ndi kutulukamo. N'chifukwa chiyani zili choncho? Chifukwa ngati simutuluka ndiye kuti simunamvere, ndipo kusam-vera n'chimodzimodzi ndi kuchita zaufiti.<sup>18</sup>

Mabungwe ndi madipatimenti ambiri amene amayendera maganizo a ku Vatican, monga a IRS, OSHA, ndiponsono Dipatimenti Yoona za Ntchito ku U.S. limodzi ndi mabungwe oona za ntchito, anawononga kolaptsa nthambi ya zachuma ya dziko lathu pakuvu-titsa ndikukakamiza anthu ambirimbiri ochita malonda kukhala kh-wakhwakhwa ndikuchititsa kuti mabizinezi a anthuwo alowe pansi.<sup>19</sup> Izi zachititsa kuti anthu mamiliyonu ambirimbiri a ku Amerika kuno asakhale pantchito ndiponsono azigona ndi njala, pomwe makampani ndi mabizinezi Vatican sakuvutika mpangóno pomwe koma kutukuka, chifukwa ndi omwe akuyendetsa zinthu m'boma. Taonani zimene Mulungu ananena zokhudza okana Kristu akadzaponyedwa ku Gehena:

**"Iwo amene akuona iwe adzayang'anitsitsa iwe, nadza- lingalira za iwe, ndi kuti, Kodi uyu ndi munthu [Wokana Kristu] amene ananthunthumirtsa dziko lapansi, amene anagwedeza maufumu; amene anapululutsa dziko, napa-sula Mizinda yake?"** (YesAya 14:16-17).

<sup>10</sup> Information Please Almanac, 1982, tsa. 98   <sup>11</sup> Smokescreens, Jack Chick, tsa. 19   <sup>12</sup> Smokescreens, Jack Chick, tsa. 35   <sup>13</sup> Double Cross, Chick Publications   <sup>14</sup> PBS Late Night Interview with Timothy Leary, July 1983   <sup>15</sup> 50 Years in the "Church" of Rome, Charles Chiniquy, tsa. 510 (orig. unabridged 1886 version, available as PDF, tsa. 359)   <sup>16</sup> Gen. Ch. 6-7   <sup>17</sup> Gen. 19:24-25   <sup>18</sup> I Sam. 15:23   <sup>19</sup> The Vatican Billions, Avro Manhattan, tsa. 214-215

## BUNGWE LA FEDS LIKUVOMEREZA ZOTI A KU VATICAN AZIG-WIRITSA NTCHITO ANTHU NGATI AKAPOLO

Imodzi mwa mabizinezi akuluakulu, a mabiliyon ambiri ya Vatican ndi yopanga mowa ndi vinyo, imene ilibe vuto lililonse la anthu antchito chifukwa chakuti imagwiritsa ntchito anthu ngati akapolo osawalipira chilichonse zimene zili zosayenela (amonke a Roma Katolika masauzande ambirimbiri). Mabungwe a boma la chitaganyawa sangalole kuti anthu ena azisangalala ndi ubwino odziperekwa panchito zathu kwa Mulungu, Atate wathu, ndiponso Mpulumutsi wathu, Ambuye Yesu Kristu chifukwa tonse ndife "achikunja" (anthu omwe si a Roma Katolika). Ndithudi, mabizinezi awo amatukuka opanda kuonongeeka kapena kukhumudwitsidwa kulikonse pogwiritsa ntchito Abale awo Achikristu osawalipira kanthu,<sup>20</sup> monga mmene zilili ndi makampani ofulula mowa a La Salle, ndi Benedictine (omwe amagwiritsa ntchito anthu ngati akapolo) ndiponso makampani ena ambiri omwe akupezeza kuyambira ku Napa Valley, California, mpaka ku New York State.

Mabungwe ndi madipatimenti a Vatican a IRS, ndi Dipatimenti Yoona za Ntchito ku U.S. tsopano adutsa malire osiyanitsa pakati pa malamulo oyendetsera dziko ndi malamulo a tchalitchi ndipo, mwa njira iliyonse, akuyesetsa kuononga matchalitchi ena Achikristu komanso masukulu m'njira zosianasiyana. Njira imodzi ndiyo kuwakkamiza kuti aziperekwa misonkho kuboma. Bungwe ili (la IRS) lomwe silifunira zabwino anthu a ku America- komanso malamulo oyendetsera dziko, kuteroku, lalamula kuti mabungwe olitsatira omwe ali ku America amene analembetsedwa pansi pa Internal Revenue Code 501(c)3, asamapereke misonkho. Bungweli silinayese n'komwe kulamula zoti nawonso aziperekwa misonkho.<sup>21</sup> Bungwe la zotolera la Aromali (la IRS) likuonetsetsango kuti tchalitchi cha Roma Katolika ndi ena onse amene amagwirizana nacho (tchalitchi chimodzi chapadzikolo) ndi gulu lokhala lachipembedzo ku U.S. limene silikuperekwa msonkho wa katundu ngakhale msonkho pa mabizinezi awo omwe ndi a ndalama mabiliyon a nkhaninkhani.<sup>22</sup> Akuchita zimenezi pansi pa Sekishoni 892 ya Internal Revenue Code (malamulo okhudza Kutolera Misonkho M'dziko). Vatican ndi chipembedzo chokhachonso chimene chimalandira madola mamiliyon ambirimbiri kuchokera kuboma chaka chilichonse kuti aziyendetsera masukulu awo.<sup>23</sup> Ndalama zimenezi zimachokera ku misonkho imene mumaperekwa. Izzi zikugwirizana ndi zimene Bishopu Wamkulu Gilroy ananena zoti, "**Tizigwirizana Akatolika tokhatokha basi**" ndi "**tigonjetse anthu onse achikunja**."

A Vatican anagwiritsa ntchito chipani cha Communist pothana ndi matchalitchi a Russian Orthodox, anagwiritsanso ntchito chipani cha Nazi pofuna kuthana ndi Ayuda komanso masunagoge awo. (Anachita izi chifukwa a ku Vatican amati anthu ena onse kupatula iwowo ndi "achikunja" — omwe si a Roma Katolika.)

### IRS-BUNGWE LA ZOTOLERA LA CHIPEMBEDZO CHA A ROMA

Gulu la Jesuit la Roma Katolika linayambitsa dongosolo losunga ndalamda padziko lonse<sup>24</sup> lotchedwa Illuminati ndiponso Agentur (ndipo limawanamizira Ayuda kuti ndi amene anayambitsa zimenezi). A Roma amayendera mfundo yakuti, "Munthu amene ali ndi matumba a ndalama amayendetsa boma." Akuluakulu a ku Vatican anayambitsa nkondo zonse (bungwe lachiroma lofufuza chikhulupiliro cha anthu) n'cholina chothana ndi aliyense padziko lonse lapansi amene amamuona kuti ndi wachikunja (anthu amene si a Roma Katolika) ndipo amabwereketsa ndalamda kwa mayiko osianasiyana kuchokera ku mabanki awo n'cholina choti akhale ndi ndalamda zokwanira pakumenyana navo. Mopusa tinalola bungwe lotolera ndalamda limeneli kuti likhazikike m'dziko lathuli (bungwe la IRS—lomwe limachita zofuna za a Roma).

Malinga ndi malamulo a Mulungu amene ali mu Baibulo, pakutha pa zaka 50 zilizonse ngongole zimene sizikanalipilidwa zimayeneleka kukhululukidwa (chithandizo kwa ovutika). Chaka chimenechi chi-

matchedwa chaka chachikondwelero (Levitiko 25:10). Motero, tiyeni tidumphe lamulo lopondereza, laukapolo ndiponso lakupha la Roma Katolika ndipo tibwelere ku lamulo la Mulungu ndi Mwana Wake, Kristu Yesu. Tiyeni tikhale ndi chikhululuko (chaka cha chikondwelero). Ngongole zimenezi amachititsa ndi satana (tchalitchi cha Roma Katolika) kuti tipwetekeke komanso kuti tikhale mu ukapolo wa zachuma. Ife si amene tinayambitsa nkondo zimenezi, ife sitinafune nkondo zimenezi, ndipo ife sitinabwerekere ndalamazo. Ndiye ife titutikirenji? Amene anayambitsa nkondo zonsezi ndi a Roma Katolika pofuna kuurnba dziko lonse lapansi kukhala boma limodzi, mpingo umodzi, ndiponos gulu limodzi lofalitsa nkhanji.<sup>25</sup>

Pamsunkhano womwe unachitikira ku Vancouver womwe cholina chake chinali kukambiranza za mmene padzikoli pangakhalire chipembedzo chimodzi chokha, ena mwa anthu athu amene anapezekapo anangoti kakasi ataona zinthu monga tinyumba toti amuna kapena akazi okhaokha azigonaniramo, mabuku olimbikitsa zoti amuna kape-na akazi okhaokha azigonana, tinyumba tochitiramo zaufiti ndiponso mabuku ofotokoza zaufitizi, kuledzera modetsa nkhwawa, komanso pankachitika zinthu zambiri zimene Mulungu amadana nazo, zimene chipembedzo chachikulu kwambirichi "chopezeka paliponse" padziko lonse chimalambira. Anthu a satana amenewa amanena kuti aliyense amene amalalikira moona Mawu a Mulungu, zimene zili zosakhudzana ndi uchimo, n'kumachita zabwino<sup>26</sup> —ankati ndi chipembedzo cha upandu. Koma anthu a Satanawa amalambira m'tsogoleri wa bungwe limene likufuna kukhala lokha padziko lonse lapansi, yemwe ndi papa...

**"Amene atsutsana nazo, nadzikuza pa zonse zotchedwa**

**Mulungu, kapena zopembedzedwa; koteru kuti iye [kapena amene akhale papa posachedwa] ngati Mulungu, [posachedwa adzakhala] mu kachisi wa Mulungu [ku Yerusalem], nadzionetsera yekha kuti ali Mulungu"** (2 Atesalonika 2:4).

**"Ngakhale iye, amene kudza kwake kuli monga mwa machitidwe a Satana ndi mphamu yonse ndi zizindikiro ndi zozizwa zonama, ndi chinyengo chonse cha kusalungama mwa iwo akuwonongeka"** (2 Atesalonika 2:9-10).

Anthu amamugwadira ndi kupsompsona mphete ndi mapazi ake<sup>27</sup> n'kumamutchula kuti "atate woyer," zomwe n'zoletsedwa mu Baibulo.<sup>28</sup> Anthu amachita zilizonse zimene iye akufuna. Akamatitchula kuti ndife a mpatuko, amene tikuyenda mu Mzimu ndi kumachita chilichonse chimene Mulungu akufuna, ayenera kuti amakhala akuchita tchimo losakhululukidwa—lomwe ndi kuchimwira Mzimu Woyer. Tchimo limeneli silingakhululukidwe m'dziko linoli komanso m'dziko limene likubweralo (Mateyu 12:31-32). Koma Satanwa sadandaula ndi zimenezi chifukwa iye anachitira kale mwano Mzimu Woyer.

### LEMBA KAPENA KUTI CHIZINDIKIRO CHA CHIROMBO

Satana amafuna zoti inuyo mukapse naye limodzi ku Gehena kwa muyaya.<sup>29</sup> Pofuna kuti inuyo mukapsedi, taonani zimene iyeyo, kudzera m'maboma komanso mabungwe osianasiyana a boma, wakhala akuchita: boma likuyesetsa kuika malamulo okuchititsani kuti mukhale ndi lemba kapena kuti chizindikiro padzanja kapena pa mphumi panu kuti muziloledwa kugula kapena kugulitsa (zimenezi zimachitika m'njira yosaonekera). Chizindikiro kapena kuti lemba limeneli Mulungu amalitchula kuti "chizindikiro cha chirombo" (Chivumbulutso 19:20). Vatican lemba kapena chizindikiro chimenechi anachipatsa mayina abwino ngati akuti "lemba kapena chizindikiro cha mtendere, chikondi, mgwirizano, chitsitsimutso, ndi ena otero." Ndipo Mulungu akutiuza kuti ngati tilandira lembali / chizindikiro chi ndiye kuti tidzapita ku Gehena (Chivumbulutso 14:9-11).

Papa, yemwe ndi bwana wamkulu, pamodzi ndi mabungwe ake a boma lachitaganya adzanena kuti ngati sitilandira chizindikiro kapena lemba limeneli ndiye kuti tidzanyanyalidwa (sitidzatha kugula kapena kugulitsa). Ine ndidzadalira Mulungu kuti adzandidyetsa,

<sup>20</sup> The Vatican Billions, Avro Manhattan, tsa. 182. <sup>21</sup> Up until 1987 mabungwe onse achikomyunizimu sankakhoma misonkho. Koma tsopano chifukwa cha nkhanji zimene ndimalemba, achotsedwa pa gulu losakhoma misonkho. Komabe, akuluakulu a ku Vatican amalowerera kwambiri m'zochita za boma ndipo amanamizira kuti iwo ndi a Republicans ndiponso a Democrats ndipo amati sipofunikanzo kuti asamakhome misonkho. Ndipo ntchito zonse zamalonda za boma zimaperekeda kumagulu awo amene amanamizira kuti ndi othandiza anthu n'kumalandira ndalamda mabiliyon ankhankhani kuti aziyendetsera masukulu awo ndi mabungwe ena tchalitchi chawo cha Katolika. <sup>22</sup> Vatican USA, Nino LoBello, tsa. 87. <sup>23</sup> Vatican USA, Nino LoBello, tsa. 79. <sup>24</sup> Vatican USA, Nino LoBello, tsa. 45-47. <sup>25</sup> Dan. 7: 8:23-25, 2 Ates. 2:3-12, Chiv. 12:12-17, Chiv. 13, 14:8-11, 15:2, 16:13-14, 16, 19, Chiv. 17, 18, 19:1-3, 11-21, 20:1-4, 7-10. <sup>26</sup> Sal. 97:10, Aro. 12:9, 1 Akor. 10:21, 2 Akor. 6:14-18, Aef. 5:3-12, Yak. 4:4, 1 Yoh. 1:5-6. <sup>27</sup> The Crisis of Church and State 1050-1300, Brian Tierney, Prentice-Hall, tsa. 49. <sup>28</sup> Mat. 23:9. <sup>29</sup> I Pet. 5:8, Chiv. 12:11-12.

monga mmene anadyetsera ana Achihebri kwa zaka 40 m'chipululu cha Sinai. Ndipo Mulungu adzachitanso zoziwitsa kwa atumiki Ake okhulupirika amene akana kutsatira papa, mabungwe ake aboma, komanso lemba la chilombo lija.

Nayenso Pulezidenti Reagan wakopeka ndi zochita zachinyengo za Vatican ngati mmene akopekeranso atsogoleri ena padzikola lapansi. Izi zadziwikiratu chifukwa cha mmene wachitira zinthu mwadzidzidzi pakutumiza nthumwi ya dziko lathu la U.S. ku nyumba yaikulu ya mahule ya a Roma Katolika (Ofesi yakumudzi komanso likulu la mpingowu).

Bwana Pulezidenti, mwanyanyatu kuchita zinthu ndi gulu la mpatukolo la Jesuit, chipembedzo chimodzi chokha padzikola lonse lapansi, ndipo akukupatsani malangizo olakwika kwambiri. Kodi ndi ndalamala zochokera ku Vatican ndiponso zambirimbiri zokutchinjirizani ku Vatican zimene zikukuchitansi kuti mulowe gulu limeneli? Kodi mungagulitse moyo wanu wamuyaya polola kuti inuyo ndi dziko lathu lilowe nawo mchitidwe Wokana Kristu chifukwa cha ndalamala komanso mphamu zakanthawi kochepa?

Ambuye akufunsa kuti, "Munthu apindulanji, akadzilemerezza dziko lonse, natayapo moyo wake [wa tuyaya]?" (Marko 8:36). Pakuchita ichi, tsopano muli pavuto loopsa ndi Mulungu wamoyo, pokhapokha mutachilikuka ndikusya zoipa n'kuvomereza pamaso pa anthu kuti simuzigwirizananso ndi Wokana Kristu n'cholinga choti Ambuye komanso anthu onse adziwe mbali imene muli.

Mokulemekezani, Bwana Pulezidenti, m'dzina la Yesu, ndikukuanzi zinthu izi. Tili m'masiku otsiriza, ndipo nthawi ya ochita ndale yatha. Tonse tikuyenera kusonyeza kwa anthu zimene zili mumtima mwathu. Baibulo limanena kuti munthu aliyense wokana chidzudzulo chocokera mu Mawu a Mulungu ndi wopulkira (Miyambo 12:1). Bwana Pulezidenti ndiponso mapulezidenti ena onse ndi mafumu onse a padzikola lapansi, kuli chiweruzo cha tonsefe, ndipo ndikukhulupirira kuti chikubwera posachedwa.

## **MWISRAELI WENIWE NI AMAKHULUPIRIRA MULUNGU**

Sikuti ine ndine wophunzira za Mawu a Mulungu wa kuseminale ayi. Ndine Mwisraeli weniweni, wosambitsidwa ndi mwazi wa Yesu, wodzazidwa ndi Mzimu Woyer, ndiponso wotumidwa ndi Ambuye kuti ndilalikire za Yesu anakomedwa pamtanda, anaukitsidwa kwa akufa, ali ndi moyo, ndipo posachedwapa adzabweranso padzikola lapansi.<sup>30</sup> Ndili ndi mphamu zonse kuchokera Kumwamba kuti ndilalikire uthenga umenewu.

Mwisraeli weniweni ndi amene amakhulupirira Mulungu, zomwe Ayuda ambiri sachita-, chifukwa anakana Mesiya pakukana malemba oposa 300 a mu Chipangano Chakale onena za Mesiya. Aisraeli ena akopedwa n'kulowa gulu la mpatuko limeneli (Roma Katolika). A Vatican akufuna kuti Aisraeli amenewa akhale marabi n'cholinga choti awatumize kunyumba ya malamulo ya ku Israeli ngati azondi. Ena mwa arabi achi Roma a Jesuit ali m'nyumba ya malamuloyi ngati azondi.

Pa nthawi ya Nkhondo Yachiwiri Yapadzikola Lonse, dziko la Poland linali la mphamu kwambiri pa mayiko amene amayendet-sedwa ndi Vatican. Ngati a ku Vatican amakonda Ayuda kwambiri—nthawi imeneyo komanso panopa—n'chifukwa chiyani analola zoti nyumba zosungiramo anthu kuti akaphedwe za Ayuda ambiri, zotchedwa maslota pens kuti zikhale ku Poland? N'chifukwa chiyani a ku Vatican anachita chinyengo ndi chikalata chodana ndi Ayuda, "Malamulo a Akuluakulu a ku Ziyoni," kudzudzula malingaliro a Vatican wofuna kuti azilamulira dziko lonse pa ifeyo Ayuda? N'chifukwa chiyani ananamizira Ayudafe zachinyengo zimene ankachita mabanki adziko lonse, iluminati ndi Agenturs?<sup>31</sup> Ndipo n'chifukwa chiyani a Vatican anaika azondi omwe akunamizira kuti ndi arabi m'nyumba ya malamulo ya ku Israel ngati anthu odana ndi Ayudawa, a chipembedzo cha Roma Katolika amakonda Ayuda kwambiri? Mulungu akuti:

**"Anthu anga inu, iwo amene akutsogolerani ndiwo  
akuchimwitsani, nawononga njira zanu" (Yesaya 3:12).**

Nthawi yoti Mesiya abwerenso kachiwiri yafika tsopano, choncho lapani kapena wonongekani,<sup>32</sup> Kutanthauza kuti mulandire Mesiya ndi kuvomereza masautso Ake, amene ali mwazi Wake, umene anakhetsa chifukwa cha machimo anu,<sup>33</sup> kapena wonongekani, kutanthauza kuti mupita ku Gehena ngati simutero.<sup>34</sup>

Pali atsogoleri a zipembedzo amene akutsogolera anthu mamiliyonu ambirimbi ku Gehena chifukwa chaubale komanso kutamandira Wokana Kristu pamodzi ndi gulu lake la mpatuko, "Kunena mabodza podzibisa makhalidwe awo oipa; olochedwa m'chikumbumtima mwa wo ndi chitsulo chamoto" (1 Timoteyo 4:2). Ena akunamizira kuti ndi Akristu koma ali Ansembe a Jesuit. Iwo ndi mabungwe awo amapatsidwa ndalamala zankhaninkhani kuchokera ku Rome chifukwa akusa unyinji wa anthu osazindikira amene amawatsatira mosakayikira kallikone kulowa mutchalitchi cha Satana cha padzikola lonse, chomwenso chili ndi mapulani oti mtsogolo muno anthu onsewo adzakhale ndi lemba la chirombo<sup>35</sup> ponamizira ngati ndi chigwirizano cha Akristu, ubale, mtendere, mphamu za uzimu, ndi chikondi. Anthu ambirimbi asocheretsedwa mosavuta kulowa mugawo ili la gulu la-chisokanezo la Vatican ndipo amaganiza kuti zonse zili bwino "**popeza chikondi cha choonadi sanachilandire, kuti akapulumutsidwe iwo**" (sanatsatire Mawu a Mulungu enieni). Chifukwa cha ichi, Mulungu wanena kuti "**atumiza kwa iwo machitidwe a kusocheretsa, kuti akhulupirire bodza: kuti onse aponyedwe ku Gahena amene sanakhulupirire choonadi, koma kukondwera ndi chosalungama [dongosolo lonse la Wokana Kristu]**" (2 Atesalonika 2:3-12).

Atsogoleri achinyengowa amakonda ndalamala za Roma Katolika ndiponso kugwirizana ndi anthu andale. Zimenezi zimawathandiza kuti azione ka m'ma TV afuko lonse komanso apadzikola lonse, ndipo zimawathandiza kuti atchuke kwa kanthawi kochepa ndi maina awo, monga ku mapulogalamu ena a pa TV, mayunesite, midzi, ndi mabizinezi ena achabechabe ndi omwe amayenera kuhala a Khristu a chikondano. Mulungu akuti:

**"Kupata chuma ndi lilime lonama ndi uchabe  
oponyedwa uku ndi uko wa iwo amene akuyang'ana imfa"**  
(Miyambo 21:6).

Atsogoleri amenewa amalemekeza komanso kugwirizana ndi upapa. Nthawi zambiri amapita kukaonana ndi papa ku Rome ndipo pafupifupi m'misonkhano yaho yonse amaitana mtsogoleri wa Roma Katolika ndikuwalora osachita manyazi n'komwe pa wailesi ya kanema (TV) ndi wailesi youlutsa mawu. Analimbikitsa Pulezidenti Reagan kusintha dziko lathu kuhala lokana Kristu (Vatican). Vatican imawalimbikitsa, ndipo amalimbikitsa Vatican chifukwa choti onse zochita zavo n'zimodzi (abodza okhaokha). Mungawaone mosavuta, ndipo ndikulupilira kuti mukuwadziwa kuti ndiayani, (ingoyatsani TV yanu).

Muzipempherera anthu akhunu amene amawatsatira chifukwa "amakhulupirira mau onama, osapindulitsa" (Yeremiya 7:8), ndipo kwa atsogoleri akhunu amenewa omwe "sanena choonadi; aphunzitsa lilime lao kunena zonama" (Yeremiya 9:5), iwowa ndi akhunu ndipo akutsogolera akhunu anzawo, pakuti Yesu ananena kuti onse adzagwera m'mbuna (Luka 6:39). Yesu ananenanso kuti:

**"Onse a mabodza, cholandira chawo chidzakhala  
m'nyanja yotentha ndi moto ndi sulfure"** (Chivumbulutso 21:8). Ndipo sadzalowa Kumwamba chifukwa "kunja kuli agalu, ndi anyanga, ndi achigololo, ndi ambanda, ndi opembedza mafano, ndi yense wakukonda ndi kuchita bodza" (Chivumbulutso 22:15), chifukwa ali ngati iye (Satana) amene ananyenga Hava ndipo panopa akunyenga dziko (imfa iliyonse inayamba ndi bodza).<sup>36</sup>

Yesu sanabweretse mtendere, koma lupanga (Mateyu 10:34). Iye anabwera kuti adzatisonyeze kusiyana kwa kuwala ndi mdima, chabwino ndi choipa, choonadi ndi bodza,

<sup>30</sup> Mat. 10:7-8, 28:18-20, Marko 16:15-20, Luka 24:46-48, Mac. 1:8-11, 10:38-43, 1 Akor. 1:17-24, 2:1-5, 9:16-17, Akol. 1:25-29, II Tim. 4:1-2. <sup>31</sup> *A History of the World*, Hugh Thomas, Harper-Row, tsa. 498; *Germany 1866-1945*, Gordon A. Craig, Oxford, tsa. 84. <sup>32</sup> Yow. 2:28-32, Mat. 24:3-51, Luka 21:7-36, II Tim. 3:1-5, I Pet. 4:7, Chiv. 6:12-17, 14:6. <sup>33</sup> Mat. 26:28, Aro. 3:22-26, 5:8-21, Akol. 1:13-14, 20-23, Heb. 9:11-14, 10:5-17. <sup>34</sup> Miy. 15:24, Mat. 3:12, 13:24-30, 37-43, 47-50, 22:13-14, 24:42-44, 48-51, Luka 3:17, 6:19-31, 13:26-28, Chiv. 20:11-15. <sup>35</sup> Chiv. 13:15-18, 14:8-11, 15:2, 16:1-2, 19:20, 20:4. <sup>36</sup> Gen. 3:4-5

thupi la Kristu ndi Wokana Kristu. Iye anati, Nkhosa Zanga zimadziwa mawu Anga ndipo zimanditsatira (Yohane 10:3-5, Chivumbulutso 14:4). Kodi inuyo mumamva mawu a Yesu kapena a papa? Kodi inuyo muli mgulu la nkhoa za Yesu kapena mbuzi za Wokana Kristu<sup>37</sup> Koma mumasangala kumva mabodza kapena choonadi (Mawu a Mulungu)?

Ambiri mwa inu mwakhala mukuthandiza Wokana Kristu popera chakhumi kubungwe lake. Yambanipo kuthandiza Kristu, osati Wokana Kristu kuti musadzapite ku Gehena kumene iyeyo adzapite chifukwa chomuthandiza kunama. Palinso gulu lachinsinsi la Vatican limene likunamizira kuti ndi Akristu ndipo likupezeka padziko lonse n'kumalowa m'matchalitchi osiyanasiyana a Pentekosite n'cholinga chotolera ndalamu zoti akamangire kachisi ku Yerusalem wa Wokana Kristu (Kachisi wa Solomo), ndipo Akristu ena omwe ndi mbuli, amene amaganiza kuti sanganyengedwe ngati Hava, akumaperekadi ndalamu m'malo mochita zinthu mozindikira n'kumaperekira chakhumi ku ntchi-to zothandiza Akristu enieni. Yesu anati, “**Anthu anga awonongeka [kupita ku Gehena] chifukwa cha kusadziwa**” (Hoseya 4:6).

Anthu amene amalankhula moimira tchalitchi cha Roma Katolika amakwiya Mawu a Mulungu akamalalikidwa ndipo amati iwo “sakhlupilira kuti tsiku lalero ndi kale anthu adakalipobe amene amalalikira udani, chinyengo, ndi tsankho, ndi zina zotero.” Koma kwenikweni zimene ma ambasada a Vatican amenewa akunena n'zakuti, iwo sangakhulupilire, tsiku lalero ndi kale, alipobe anthu olalikira Mawu a Mulungu, choonadi, ndikuti padakali anthu olimba mtima amene akuvumbula ntchito za Satana (iwovo). Zipembedzo zina zimene poopa kutha zinalumikizana ndi Vatican zinanena kuti “palibe pamene m'Baibulo, pakusonyeza Mulungu kapena Mwana Wake, Kristu Yesu, kuti anayankha, kapena kuuza ana awo kuti ayankhe.”

Mu Baibulo, kuyambira m'buku la Genesis mpaka la Chivumbulutso—Mulungu, Mwana Wake Kristu Yesu, anthu akale okhulupirika, aneneri, ophunzira, ndiponso atumwi ankamuyankha Satana pa mfundo iliyonse, nthawi iliyonse imene akumana ndi chipunzitsa cha Satanayo chabodza.<sup>38</sup> Yesu anatilamula kuti tizigwiritsa ntchito lupanga (Mawu a Mulungu) potetezera ndi kusunga Uthenga Wabwino pomuyankha Satana (pa mfundo iliyonse) mwakhama ndiponso molimba mtima.<sup>39</sup> Tinalamulidwa kuyankha bodza la Satana (akamapotoza Mawu a Mulungu) potsanzira Yesu pamene ankayankha mdyerekezi pa Phiri la Mayesero (Mateyu 4:3-11).

Paulo, motsogozedwa ndi Mzimu Woyer, ananena kuti, “Lalikirani mawu,” Mawu onse (2 Timoteyo 4:2). Osasiya malemba okhudza Wokana Kristu, aneneri onyenga, kuyankha anthu abodza, kudzudzula, ndiponso kulangiza. Yesu ananena kuti timakhala ndi moyo (kupita Kumwamba) ndi Mawu aliwonse otuluka m'kamwa mwa Mulungu (Mateyu 4:4). Izi zikutanthauza mawu onena za Wokana Kristu, aneneri onyenga, ndi ena otero, chifukwa Yesu ananena kuti tikadziwa choonadi (choonadi chonse, liwu lonse), choonadi chidzatimasula (Yohane 8:32). Koma Wokana Kristu ndi aneneri ake onyenga sakufuna kuti mumasuke chifukwa mbuye wawo ndi Satana, amene amakonda kuchititsa anthu kuhala muukapolo. Ngati iwo sakufuna kuti anthu akhale mu ukapolo, ndiye n'chifukwa chiyani amakwiya Mawu onse a Mulungu akamalalikiridwa (omwe amamasula anthu kwa Satana)? Ndipo n'chifukwa chiyani amanena kuti kulalikira Mawu onse n'koipa, kumayambitsa chidani, kusagwirizana ndiponso tsankho ngati sali ochokera kwa Satana?

Wokana Kristu ndi aneneri ake onyenga amanena kuti sitikuyenera kuchita chilichonse—pa nkhanu yotumikira Mulungu—ndi mtima wonse. Iwo amati kusunga malamulo a Mulungu, kulalikira ndi kuchita Mawu a Mulungu ndi mtima wonse ndi tchimo. Koma m'buku la Chivumbulutso, Yesu anatilamula kuti tizitumikira Mulungu mwakhama kupanda kutero adzatilavula mkamwa Mwake (Chivumbulutso 3:16). Khama ndi kulimba mtima (mtima wonse) ndi malamulo a Mulungu ndi wodzozedwa Wake. Tinalamulidwa kuchita zinthu zonse zimene tikuchita, mwa Ambuye (Akolose 3:23)

ndi mtima wonse (Mateyu 22:37), ndiponso mwakhama (mtima wonse). Ndipo ngati anthu akukwiya chifukwa cha Mawu a Mulungu (mawu aliwonse), Mulungu akuti anthu amenewo ndi ankhanza (ngati zirombo). Ndipo Mulungu akutinso kukhumudwa kapena kukana Mawu Ake ndi tchimo.<sup>40</sup> Kukana Mawu a Mulungu n'chimodzimodzi ndi kukana Kristu, ndipo tingapulumutsidwe kudzera mu kuvomeriza (kukhulupirira) Mawu, omwe ndi Kristu. “**Ukhulupirire mwa Ambuye Yesu [Mawu], ndipo udzapulumuka**” (Machitidwe 16:31).

Vatican, kudzera mugulu lake la Mafia, moyamba anawononga dziko ndi zithunzi zolaula, uhule, mankhwala osokoneza bongo, kufulula ndi kugulitsa mowa, ndi zina zotero. Panopa akunamizira ngati si iwowa amene amalimbikitsa zinthu zimenezi, akufuna kubweretsa malamulo a sensashipi pa zonyasa zimene iye anaziyambitsa yekha m'dziklo lathu komanso padziko lonse lapansi.

Iyi ndi njira yachinyengo, yoipa kwambiri ya gulu la mpatuko limeneli, yokuchititsani kukhulupirira kuti ndi labwino, laulemu, loyera, ndiponso langwiro pa za Uzimu. Ukunso kunali kuyesa koyamba kuchita sensashipi yadziklo lonse.<sup>41</sup> Cholina chake chachiwiri ndi sensashipi imeneyi n'choti aziunika zonse zimene anthu amalankhula, kuphatikizapo za mu Baibulo—kupatula zamu Baibulo zimene iwovo akufunira zilalikidwe, zimene zili zosiyananiratu ndi Baibulo.<sup>42</sup> Gulu la mpatukoli likudziwa kuti dziko lapansi silikudziwa zinthu zausata zimene likuchita, ndi dziko lonse lapansi—lomwe silikudziwa kuti zoipazi zinayambitsidwa ndi gulu lampatukoli—adzalichemerera ndi kumalilambira chifukwa cha mchitidwe ooneka “wachikoka” koma uli wachinyengowu. Akuchita zimenezi n'cholina choti akope munthu aliyense amene sasamala za iwo kuti azikhala kutali ndi Ambuye koma mwa iwo wokha.

Zolina zake zamtsogolo zimene alinazo pa anthu akhungu amenewa ndi Gehena. Chiphsyinjo chimakonda khamu, ndipo Satana ndiomutsatira ake sakufuna kuti adzapse wokha. Iwo akufunitsitsa inuyo, mtima wabwino, mudzazunzike limodzi ndi iwo kwamuyaya ku moto wolusa wa Gehena.<sup>43</sup> Kodi mukufuna zimene iwo akufuna kuti zikuchitikireni? Kapena mukufuna zimene Yesu wakukonzerani, zomwe ndi moyo wosatha pamodzi Naye kutali ndi mavuto wonse, kutali ndi zonse zachinyengo, ndiponso kutali ndi zothekera zonse za mtundu uliwonse owononga<sup>44</sup>

## KONZANI UBWENZI WANU NDI MULUNGU

Pewani kukhala ndi moyo motsatira zimene zikuchitika m'dzikoli, zomwe n'zakanthawi kochepa.<sup>45</sup> Konzani tsogolo lanu mosatha pophunzira zimene Mlengi yemwenso ndi Wolamulirawa dziko lonse wakukonzerani—Pakukana kugwirizana ndi mapulani a gulu la mpatuko la Satanali akuti satana ndi anthu ake a Roma Katolika azilamulira dziko lonse zimene zili zopanda pake ndi zachidule.<sup>46</sup> Mukapanda kutero, mumusonyeza Mulungu kuti nanunso ndinu ausata ndiosamvera ngati oipa ameneyu yemwe amadzitchula kuti ndi wamsembe wa Mulungu, “mulungu” mwini padziko lonse. Khalani m'chiyero ndi Mulungu—panopa nthawi isanathe (ngati mmene yamuthelera mdyerekezi). Utsi wake wochokera ku Gehena udzakwera kumwamba mpaka tuyaya (Chivumbulutso 14:11).

**“Bwerani tsopano, tiyeni tipange mfumdo limodzi, ati**

**Yehova; ngakhale machimo atakhala ofiira, adzayera ngati matalala; ngakhale atakhala ofiira ngati kapezi, adzakhala ngati ubweya” kudzera m'mwazi wa Yesu (Yesaya 1:18).**

Mchikondi cha Mulungu, anatumiza kudzatifera ife chomwe amachikonda kwambiri (Mwana wake). Yesu amatikonda kwambiri moti analolera kutaya moyo Wake ndikukheteta mwazi Wake chifukwa cha ife, n'cholina choti machimo athu achotsedwe, akhululukidwe.<sup>47</sup> Ngati tili ndi chikondi chofanana ndi chimene Mulungu ndi Mwana Wake, Kristu Yesu, anatisonyeza, tidzasiya machimo ndi njira zathu zoipa, tidzaphunzira Mawu a Mulungu molondola, tidzauza dzikoli choonadi chake chomwe akhala akunamizidwa kwa nthawi yaitali—

<sup>37</sup> Mat. 25:31-46, Yoh. 10:1-16, 26-28   <sup>38</sup> Mat. 4:3-11, 16:21-23, Chiv. 22:18-19   <sup>39</sup> Aef. 4:27, 6:17, 2 Ates. 2:14-15, II Tim. 1:13, Tito 3:10, Heb. 4:12, Yak. 4:7   <sup>40</sup> Ezek. 20:21-24, Zek. 7:11-13, Yak. 2:10-11, I Yoh. 3:4   <sup>41</sup> Church and State, Vol. 37, No. 1, Jan. 1984, tsa. 16   <sup>42</sup> The Vatican Empire, Nino LoBello, tsa. 68   <sup>43</sup> Mat. 22:13, 25:30-46, Marko 9:43-44, Luka 3:17, 2 Ates. 1:1-9, II Pet. 2:4, 9, Chiv. 14:10-11   <sup>44</sup> Isa. 64:4, 1 Akor. 2:9, Chiv. 7:16-17, 21:3-4, 22-27, 22:1-5   <sup>45</sup> Sal. 103:15-18, Yoh. 12:25, Yak. 1:9-12, 1 Yoh. 2:15-17   <sup>46</sup> Dan. 7:7-11, 23-26, Chiv. 14:8, 16:10-11, 17:15-18, Ch. 18, 19:20   <sup>47</sup> Mat. 26:28, Mac. 13:38-39, Heb. 9:22, 26, 1 Yoh. 1:7

n'cholinga choti nawonso adzapeze moyo umene Mulungu ndi Mwana Wake auperekwa kwa ulele. Koma angadziwe bwanji ngati palibe wowalalikira (osati wongoyamba kumene, koma iye amene waphunziradi njira zonse za Ambuye)?<sup>48</sup>

**"Koma ngati mukana ndi kupanduka, mudzathedwa ndi lupanga: chifukwa m'kamwa mwa Yehova mwatero"**  
(Yesaya 1:20).

Ngati mukufuna kupulumutsidwa, nenani pempheroli ndipo mudzapulumukadi:

**AMBUYE wanga ndi MULUNGU wanga, chitirani chifundo mzimu wanga, wochimwa.**<sup>49</sup> Ndikukhulupirira kuti YESU KRISTU ndi MWANA wa MULUNGU wamoyo.<sup>50</sup> Ndikukhulupirira zoti IYE anafera pamtanda ndipo mwazi WAKE wamtengo wapatali unakhetesdwa kuti machimo anga onse akhululukidwe.<sup>51</sup> Ndikukhulupirira zoti MULUNGU anaukitsa YESU kwa akufa ndi mphamu ya MZIMU WOYERA,<sup>52</sup> ndipo panopa IYE wakhala kudzanja lamanja la MULUNGU ndipo akumvetsera pemphero langa lolapa machimo anga ndi pempheroli.<sup>53</sup> Ndikutsegula zitseko za mtima wanga, ndipo ndikukuitanani INU AMBUYE YESU, kuti mulowe mu mtima mwanga.<sup>54</sup> Ndisambitseni machimo anga onse oipa kwambiri pogwiritsa ntchito mwazi wanu wamtengo wapatali umene unakhetesdwa pamtanda wa Kavari.<sup>55</sup> INU simudzandikana, AMBUYE YESU; INU mudzandikhululukira machimo anga ndi kupulumutsa moyo wanga. Ndikukhulupirira zimenezi chifukwa MAWU ANU, Baibulo amanena zimenezi.<sup>56</sup> MAWU ANU amati INUYO simudzakana aliyense, ndipo aliyenseyo akuphatikizapo ineyo<sup>57</sup> Choncho, ndikudziwa kuti INUYO mukundimva, ndipo ndikudziwano kuti INUYO mwandiyankha, komanso ndikudziwa kuti ndapulumuka.<sup>58</sup> Ndipo ndikukuthokozani INU, AMBUYE YESU, pondipulumutsa, ndipo ndisonyeza kuyamikira kwanga pochita zonse zimene INUYO mukufuna ndipo sindidzachimwano.<sup>59</sup>

Munthu akalandira chipulumutso, YESU ananena kuti azibatizidwa, pomizidwa thupi lonse m'madzi, m'dzina la ATATE, ndi la MWANA, ndi la MZIMU WOYERA.<sup>60</sup> Muziphunzira mwakhama Baibulo Buku Lopatulika la KJV, ndipo muzichita zimene limanena.<sup>61</sup>

AMBUYE akufuna kuti Inuyo muziuza ena za chipulumutso chanu. Mukhonza kumagawa nkhanzi za Uthenga Wabwino zimene M'busa Tony Alamo amalemba. Tizikutumizirani nkhanizi komanso mabuku mwa ulere. Tiimbireni foni kapena tilembereni imelo kuti mumve zambiri. Mungauzeno ena uthenga umenewu.

Ngati mukufuna dziko lipulumutsidwe, monga mmene YESU analamulira, musamamubere MULUNGU chakhumi CHAKE. MULUNGU anati "Kodi munthu adzalandza za MULUNGU? ndipo inu mundilanda INE. Koma mukuti, Takulandani motani INU? Limodzi limodzi la magawo khumi ndi zopereka. Mutembereredwa ndi temberero; pakuti mundilanda INE, ngakhale mtundu uwu wonse [ndidziko lonse]. Mubwere nalo limodzi limodzi lonse la khumi ['chakhumi' ndi 10 pa 100 yamalipro anu] ku nyumba yosungiramo, kuti mukhale nyama [chakudya cha uzimu] m'nyumba MWANGA [miyoyo kupulumutsidwa], ndipo mundiyese tsono, ati YEHOVA wa MAKAMU, ngati sindikutseguliranai mazenera a Kumwamba, ndi kukutsanuliranai mdalitso, wakuti adzaweweka malo akuulandilira. Ndipo ndidzadzudzula olusa chifukwa cha inu, ndipo sadzawononga zipatso za nthaka yanu; ngakhale mpesa wanu sudzayoyoka zipatso zake zosacha m'munda, ati YEHOVA wa MAKAMU. Ndipo amitundu yonse adzatcha inu odala: pakuti mudzakhala dziko lokondweretsa, ati YEHOVA wa MAKAMU" (Malaki 3:8-12).

### ZINSINSI ZINANZO ZA PAPA

Vatican amachita zinthu mwachinsinsi kwambiri moti ambari mwa ansembe, asisitere ndiponiso mamembala ena a maudindo ang'onoang'ono amene amagwira ntchito ndi mabungwe aboma sadziwa n'komwe kuti ali m'gulu lalikulu zedi lochita zinthu zambiri zoipa, ndipo

kuti mankhwala osokoneza bongo, uhule, zithunzi zamaliseche ndi zolaula, mowa, ndi kusintha ndalamwa mwachinyengo—ndi zinthu zonse zoipa kwambiri—zikhonza kupezekwa kuti ndizaku Vatican ndi mabungwe ake aboma.<sup>62</sup> Anthu amene achoka m'tchalitchi chachikuluchi, cha Roma Katolika, amanena kuti 68 pa 100 ya akuluakulu aku Vatican ali ndi milandu yokhudzana ndi kugonana ndi amuna anzawo, akazi anzawo, ndiponiso kuchita chigololo. Zinthu zonsezi zimaletsedwa ndi Mulungu ndipo anthu amene amachita zimenezi adzapita ku Gehena akapanda kulapa.<sup>63</sup> Kuyambira kale kwambiri, anthu ambiri odziwika bwino akhala akunena Vatican kuti ndi "ofesa mbewu zoipa."

Wansembe wakale wa Jesuit yemwe kwa zaka zambiri anali ndi udindo wauku ku Vatican ndipo ankachita lipoti mwachindunjii kwa papa pa za mmene akugwirira ntchito yake, anandiuza kuti pa nthawi imene Papa Yohane Paulo Wachiwiri yemwe alipo panopayu anali wansembe ku Krakow m'dziko la Poland, anthu ogwira ntchito kufakitale sankasangalala ndi papa wa m'tsogoloyo (Yohane Paulo Wachiwiri). Zinamveka kuti anthu ambiri ogwira ntchito m'mafakitalike ankafuna kumupha, ndipo ankananwa kuti sakumufuna n'komwe. Yohane Pauloyu ankati akafika m'dera la anthuwo, ancamugenda ndi masanza othimbirira ndi mafuta chifukwa choti zinkamveka kuti iyeyo ankagwiririra ana awo ang'onoang'ono. Anthuwo ananenanso kuti (Papa wapanopa Yohane Paulo Wachiwiri) amachita zachiwerewere ndi amuna anzake. Izi zikuchitira umboni malamulo aboma la Vatican atsopano okhudza zolimbikitsa kuti anthu ogona ndi amuna kapena akazi anzawo asamasalidwe.

M'buku lonena za chikondi (chilakolako chogonana) limene Papa Yohane Paulo Wachiwiri analomba pa nthawi imene anali wansembe, iye anagwira mawu a Sigmund Freud mobwerezabwerezwa ngati kuti akugwira mawu amalemba opatulika. Sigmund Freud ndi Myuda yemwe analowa tchalitchi cha Roma Katolika, ndipo ndi wodziwika bwino kwambiri padziko lonse kuti ndi munthu wokonda chiwerere monyansa zedi. Satana, kudzera mu boma limodzi lolamula dziko lonse la Vatican, tchalitchi, ndi nyumba zofalitsa nkhanzi, akugwiritsa ntchito Myuda ameneyu, pamodzi ndi anthu ena amene amati ndi ophunzira m'dzikoli, pochititsa anthu kuganiza kuti "tchimo" kapena kuti "kulakwa" kulibe. Vatican akugwiritsa ntchito anthu omwe amati ndi ophunzira kwambiri komanso organiza kwambiri pokopa anthu amene amati amakhulupirira ntchito zodabwitsa zimene Mulungu amachitira anthu kalelo komanso panopa. Anthu amenewa pamodzi ndi nyumba zotchuka zofalitsa nkhanzi zimene zimayendera maganizo a ku Vatican zimanyoza munthu aliyense amene amawavumbula ku zochita zoipa za chipembedzo champatukochi pogwiritsa ntchito Mawu a Mulungu. Chipembedzo chimenechi Mulungu amachitchula m'buku la Chivumbulutso kuti ndi "hule," ndipo aliyense amene amayesetsa kutsatira zimene Mawu onse a Mulungu amanena, kuphatikizapo lamulo la Kristu la kuukitsa akufa, kuchiritsa odwala, kutulutsa ziwanda, kubadwanso mwatsopano, kukana ndi kuyalutsa zochita za mdyerekezi (hule lotchulidwa m'buku la Chivumbulutso). Zochita za uchisembwere za Yohane Paulo Wachiwiri ndi za Freud zinali zofanana, monga mmene analembera m'buku lake.

Popeza tsopano ali ndi "mphamu zambiri" (mtsogoleri wa Roma Katolika ndi mabungwe aboma osianasiyana), akutha kupanga malamulo ogwirizana ndi zimene iyeyo akufuna. Tsopano akufuna kuti anthu onse azitsatira zimene iyeyo akufuna popanga malamulo okakamiza anyamata ndi atsikana kuti azigwiritsa ntchito chimbusdi chimodzi m'zipinda zogona ku makoleji. Iye amasangalala zedi akaona mtundu wonse wa anthu ukukakamizidwa ndi malamulo kuti azichita zimene iyeyo akufuna. Malamulo atsopano a Roma okakamiza ndi akupha amenewa amalimbikitsidwa ndi awiri mwa mabungwe ake aboma otchedwa Dipatimenti Yonna za Nyumba ndi Chitukuko cha M'matauni komanso Dipatimenti ya Zamaphunziro,<sup>64</sup> zimenezi zikuoneka zantchito, ndipo amadzibisilamo ngati mmene Vatican

48 Aro. 10:14    49 Sal. 51:5, Aro. 3:10-12, 23    50 Mat. 26:63-64, 27:54, Luka 1:30-33, Yoh. 9:35-37, Aro. 1:3-4    51 Mac. 4:12, 20:28, Aro. 3:25, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 5:9    52 Sal. 16:9-10, Mat. 28:5-7, Marko 16:9, 12, 14, Yoh. 2:19, 21, 10:17-18, 11:25, Mac. 2:24, 3:15, Aro. 8:11, 1 Akor. 15:3-7    53 Luka 22:69, Mac. 2:25-36, Aheb. 10:12-13    54 1 Akor. 3:16, Chiv. 3:20    55 Aef. 2:13-22, Aheb. 9:22, 13:12, 20-21, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 1:5, 7:14    56 Mat. 26:28, Mac. 2:21, 4:12, Aef. 1:7, Akor. 1:14    57 Mat. 21:22, Yoh. 6:35, 37-40, Aro. 10:13    58 Aheb. 11:6    59 Yoh. 5:14, 8:11, Aro. 6:4, 1 Akor. 15:10, Chiv. 7:14, 22:14    60 Mat. 28:18-20, Yoh. 3:5, Mac. 2:38, 19:3-5    61 Deut. 4:29, 13:4, 26:16, Yos. 1:8, 22:5, 2 Tim. 2:15, 3:14-17, Yak. 1:22-25, Chiv. 3:18    62 Chiv. 17:1-6, 18:2-3, 23-24    63 Mat. 15:18-20, Aro. 1:20-32, 1 Akor. 6:9-10, 18, 10:8, Aef. 5:5, Aheb. 12:16-17, 13:4, Chiv. 21:8    64 Vatican USA, Nino LoBello, tsia. 78-79

imachitira podzionetsa ngati Oyera Ngati Chipale Chofewa.

Pa nkondo yauzimu yomwe ili pakati pa Mulungu ndi Satana, ndife osangalala kwambiri chifukwa Yesu anati, "Mphotho yanu ndi yaikulu m'Mwamba: pakuti potero anazunza aneneri anakhalawo musanabadwe inu" (Mateyu 5:12). Ifeyo ndi gulu lolimba kwambiri la Chikristu padziko lonse lapansi (ndipo timayinyadira mfundoyi).

Mabuku a anthu ena achinyengo amene amanamizira ngati abwino (omwenso mwachinyengo amatha kusindikiza Baibulo) samvera lamulo la Yesu lakuti, "Musawopse, musanamize munthu aliyense" (Luka 3:14), ndipo m'mabuku awo, ifeyo atika pa gulu la ampatuko. Ndipo chifukwa cha mabodza awo a mkunkhuniza ndipo chifukwa chakuti ife timayesetsa kugwira ntchito ya Ambuye mokhulupirika, tiyenera kusamala kwambiri ndi mabuku achinyengowa, ndipo tiziwaona kuti akuchokera kugulu logwirizana ndi akuluakulu a Katolika ku Vatican.

**"Muti bwanji inu, amene mupsinja anthu anga, ndi kupera nkhope ya wosauka? ati Ambuye Yehova wa makamu"** (Yesaya 3:15).

Kodi simukudziwa zoti "chimene munthu achifesa, chimenenso adzachituta" (Agalatiya 6:7)? Ndipo Mulungu adzakuchitirani zogwirizana ndi zimene inuyo mumachitira anthu ena... "Kubwezera kuli kwanga, Ine ndidzabwezera, ati Ambuye," "Ine ndidzabwezera" (Aroma 12:19, Ahebri 10:30).

Ndife okondwa podziwa kuti mphoto yathu ndi yaikulu chifukwa cha mabodza amene akhala akutinenera (Yesu ananena zimenezi) (Mateyu 5:11-12).

Maboma ndiponso nthambi zake zimene zimayendera maganizo a Vatican mogwirizana ndi nyumba zotchuka zofalitsa nkhanzi (mu kon-sati) achitsanso kuti ifeyo tikhale osangalala ndiponso kuti mphoto yathu ikhale yaikulu Kumwamba. Zili choncho chifukwa mogwirizana, atitengerapo kumakhoti pa milandu yotinamizira ndipo akhala akuyesetsa kutipekera nkhanzi<sup>65</sup> mobwerezabwereza pa zaka 15 zapitazi. Kafukufuku wathu wasonyeza kuti nyumba zotchuka zofalitsa nkhanzi,<sup>66</sup> pamodzi ndi maboma komanso nthambi zake zomwe zimayendetsedwa mwachinsinsi ndi akuluakulu a Vatican ndi zimene zikutibweretsera mavutowa. Tikukuyamikirani ndikukutamandani Inu, Yesu, chifukwa chotisoneyeza mfundo zimenezi zomwe zikutitsimikizira kuti tidzalandiradi mphoto yathu. Wamasalimo Davide analembra kuti:

**"Adzikazikitsa mafumu a dziko lapansi, Nachita upo akulu pamodzi, Kutsutsana naye Yehova, ndi Wodzozedwa wake, ndi kuti, Tidule zomangira zavo, Titaye nsinga zavo. Iye (Mulungu) wokhala m'mwambayo adzaseka; Ambuye adzawanyoza. Pomwepo adzalankhula nawo mu mkwiyo wake, Nadzawaopsa m'ukali wake"** (Salimo 2:2-5).

## **CHILANGO CHOOPSA KWAMBIRI KWA ONSE OLIMBANA NDI MULUNGU**

Muzipempherera anthu atsoka awa omwe akulimbana ndi Mulungu m'mapempherera anu, Mwana Wake, Kristu Yesu, Mzimu Woyer, ndiponso anthu odzozedwa a Mulungu, chifukwa akapitiriza zimene akuchitazi, adzalandira chilango choopsa kwambiri. Ifeyo, mofanana ndi Atate wathu wa Kumwamba, ndi Mwana Wake, Kristu Yesu, sitikufuna kuti anthu ena adzapite ku Gehena. N'chifukwa chake tikulangiza anthu onse kuti azipempherera m'dzina la Ambuye Yesu Kristu n'cholinga choti Kristu akhale Mpulumutsi waho ndikuyamba kuchita zabwino pomutumikira m'malo mochita zinthu zoipa, zomwe mapeto ake ndi Gehena osatha ndi chilango chamuyaya. (Koma sikuti timapempherera mdyerekezi kapena amene amanyoza Mzimu Woyer, oterewa sitiwapempherera [1 Yohane 5:16]). Tchalitchi chathu chaonjezereka ndi kukula ndimphamu kuposa kale monga mmene Yesu ananenera pansi pamasautso. Ngati Mulungu anakonda dziko lapansi, kodi ifenso sitikuyenera kulikonda? Nkhaniyi yalembedwa chifukwa cha chikondi n'cholinga choti anthu oona mtima asanyengedwebe ndi Vatican ndiponso anthu amene amagwirizana naye, asalandire lemba la chilombo, ndikupita ku Gehena.<sup>67</sup>

Aliyense amene anatulukira mfundo za gulu laupanduli (gulu la upandu la a Roma Katolika) ndi olitsatira ake kuyambira kale, mpakanila lero, akutchulidwa achikunja, amwano, woopsa, wobisa, wosasinta chikhulupiliro cha chipembedzo chawo, ndi zina zotero, ndipo akhala akuphedwa kumisonkhano yake imene imapha anthu ambiri.

Amanenanso zoti ifeyo tili ndi vuto lodana ndi Vatican. Kodi Abraham Lincoln ndi John F. Kennedy ankadana ndi Vatican? Ndipo anthu mamiliyonu ambirimbiri lero amene akuvutitsidwa ndi kuzunzidwa ndi maboma komanso mabungwe amene amagwirizana ndi Vatican ndiponso omwe Sali pa ntchito ndipo ndi anjala (ena ali m'ndende atakakamizika kuba chifukwa cha njala), kodi nawonso ali ndi vuto lodana ndi Vatican?

Chifukwa cha nkhanzi imene ndalembayi, gulu laupandu la Roma Katolika liyamba kudandaula ngati kuti (mwa anthu onse) likuzunzidwa, ndipo lizinena ngati losalakwa kuti, "N'chifukwa chiyani zimenezi zikutichitikira?" kudziwa kuti iwo amene akukana zinthu zachinyengo zimene tchalitchichi chimachita aziwamvera chisoni. (Ine sindingamvere chisoni mdyerekezi.) Ine sindinalembe mawu a Mulungu, koma ndiman-gowalalikira basi. Mulungu sadana ndi chabwino, koma choipa chokha.<sup>68</sup>

Vatican pamodzi ndi anthu ake onse akufunika kupatsidwa mphoto monga akatswiri onamiza anthu podzionetsa ngati iwovo ndi anthu oyera ndiponso opatalika, ndiponso chifukwa chotchena ndi kuziphoda bwino, n'kumaoneka kunja kwake ngati Oyera ngati Chipale. Mkatizwa zovala zavo zoyeria ngati Chipale, muli zilonda ndi zipere zonyeka zedi. Pamaso amakumwetuliranu mokoma n'kumati "Ndimakundama, m'bale," koma kumbuyo kwavo, amabisa manja amene amakhetza mwazi wa anthu amene amamenyelera nkondo ya chilungamo.<sup>69</sup>

Taonani chitsanzo ichi chosonyeza mmene Vatican amadzbisira nthawi zonse. Ataona kuti anagonja pa Nkhondo Yachiwiri Yapadzikolo Lonse (yomwenso inayambitsidwa ndi Vatican), mwamsanga anabisa, Ayuda 1000, pa nthawi imodzi kuti, akapha Ayuda 6,000,000, anene kuti, "Ife tinabiswa ndi kuteteza Ayuda; timakonda Ayuda ife." Izi ndiye zoonza zake zimene Vatican anachita.

Ponena za kulandira mphoto zikuluzikulu, Vatican yakhala ili mu bizinezi yopanga mafilimbu kwa nthawi yaitali.<sup>70</sup> Anthu a ku Hollywood, motsogoleredwa ndi a Roma Katolika omwe ali ndi mphamvu m'boma, amatipangira mafilimbu monga a "The Song of Bernadette," "Going My Way," ndiponso mafilimbu ena ambiri osangalatsa omwe amatamanda gulu la mpatuko limeneli la Roma Katolika. Kumbali inayi, amakamiza mafilimbu ngati "Elmer Gantry," kuwonetsa atsogoleri kapena abusa achinyengo a matchalitchi amene amatsutsana ndi utsogoleri wa papa. Kodi mukukumbukira "Dragnet" pa wailesi ya kanema? Mkristu nthawi iliyonse amamujambula atatenga Baibulo lalikulu, akumwetulira pambuyo poti wapha agogo ake kuchipinda china.<sup>71</sup> Ndipo nthawi zonse ansembe anali otchuka olemekezedwa zedi, olandira ndalamza zambiri ngati Bing Crosby ndi Barry Fitzgerald. Mwaona, tikukhudzika ndi zichitchito zambiri zimene Vatican ikuchita (mtsogoleri wa chipembedzo chimodzi padziko lonse ndi maboma onse padziko lonse).

Pamene akupitiriza kunamizira kuti azione kabe Woyeria ngati Chipale, Vatican ikugwirtsia ntchito nyumba zake zofalitsa nkhanzi kutukulira msonkhano waho wokamba zabodza wa maola atatu wa CBS ochemelera ndi kumuyeretsa papa, yemwe ndi mtsogoleri wa gulu la upandu la mpatukoli kuti aziwoneka ngati mulungu. Ndiukhulupirira kuti nkhanzi yoponya sanza lamafuta inasiyidwa.

M'chipembedzo cha Roma Katolikali muli anthu ambiri abwino omwe si olemera, ndipo ena ndi osauka kwambiri, komanso safuna maudindo akuluakulu. Ambiri mwa anthu amenewa ndi odzichepeta. Anthu wamba amenewa sadziwa mpang'ono pomwe zoipa zimene gulu lawo la mpatuko la Roma Katolika linachita ndipo likuchita, zomwe anauzidwa kuti ndi tchalitchi. Popeza Mulungu amadziwa mitima yaho yabwino (Iye ndi Mulungu wa mitima yathu), akuwauza anthu osalabadiwala kuti "**Tulukani m'menemo, anthu Anga**" (**Chivumbulutso 18:4**). Choncho tiyeni tipemphere kuti atero posachedwa.

<sup>65</sup> Vatican Imperialism in the Twentieth Century, Avro Manhattan, tsa. 155    <sup>66</sup> The Documents of Vatican II, Walter M. Abbott, S.J., tsa. 319-331; Vatican Imperialism in the Twentieth Century, Avro Manhattan, tsa. 150; The Rockefeller File, Gary Allen, Ch. 6; None Dare Call It Conspiracy, Gary Allen, Ch. 5; Collier's National Encyclopedia, 1936, s.v. "Illuminati," Catholic Encyclopedia, s.v. "Illuminati," Ingolstadt"    <sup>67</sup> Chiv. 13:16-18, 14:9-11, 19:20    <sup>68</sup> Sal. 7:11, 45:6-7, Miy. 8:13, Amosi 5:15, Aro. 1:18, Aheb. 1:8-9    <sup>69</sup> Chiv. 17:1-6, Ch. 18    <sup>70</sup> Vatican USA, Nino LoBello, tsa. 20-21

Tikumbutsenso bwana wamkulu wa Satana (papa) amene amayang'anira nyumba ya mahule ya Roma ndi maboma amene amapatsa mphamvu, kuti nthawi yako yoti ulamulire yatsala pang'ono kutha, akutero Ambuye.

**"Pakuti m'ora limodzi chasanduka bwinja chuma chachikulu chotere"** (Chivumbulutso 18:17).

**"Ndipo utsi wake ukwera ku nthawi za nthawi"** (Chivumbulutso 19:3).

**"Ndipo ndinaona motuluka m'kamwa mwa chinjoka, ndi m'kamwa mwa chirombo, ndi m'kamwa mwa mneneri wonyenga mizimu itatu yonyansa, ngati achule"** (Chivumbulutso 16:13).

Unsembe wa Ayuda unathera pa Kavari,<sup>72</sup> ndipo palibe mu Baibulo pamene Mulungu anapereka mphamvu yaunsembe kwa anthu a ku Italy, Poland, kapena anthu ochokera m'mitundu ina, yosakhala Ayuda. Ndipo pa mafuko 12 a Chiyuda, ndi fuko la Levi lokha limene Mulungu anatulutsako ansembe.<sup>73</sup> Izi zikusonyezeratu kuti zimene Vatican akuchita n'zosagwirizana ndi malemba ndipo akukhala m'moyo wapamwamba ndi wabodza. Pamene Yesu anena kuti "Kwatha," Yesu anakhala Mkulu wa Ansembe yekhayo (Yohane 19:30).<sup>74</sup>

Vatican akufuna kusamuka kuchoka ku Rome kupita ku Yerusalem. Pa September 26, 1973, Houston Chronicle inalengeza kuti munthu wina wokonda udindo wa zandale dzina lake Henry Kissinger anathandiza gulu la mpatuko lotchukali (Vatican) popereka maganizo ake "Kuti Yerusalem ukhale mzinda wadziko lonse ndipo papa aziteteza malo opatulika komanso kuyang'anira chipembedzo."

Baibulo silitchula n'komwe za purigatoliyo kapena malo ena ngati amenewa, koma Baibulo limanena mosapita m'mbali kuti, "**Kwaiki-katu kwa anthu kufa kamodzi, ndipo atafa, chiweruziro**" (Ahebri 9:27). Ndipo Mulungu ananena kuti, ndi pakati pa Kumwamba kapena ku Gehena, palibenso kwina.<sup>75</sup> Munthu sangaperekе zipphuphu kuti achoke ku Gehena.

Ndipo palibe paliponse mu Chipangano Chatsopano pamene pamanena kuti muzipha anthu amene amakhulupirira zinthu zosiyana ndi zimene inuyo mumakhulupirira. Vatican, komabe, amakutchula kupha kumeneku "nkhondo yopatulika" ndipo amaloleza kuchita zimenezi, kusonyezeratu kuti gulu limeneli ndi la mpatuko ndipo limachita zinthu zosagwirizana ndi malemba.

72 Isa. 53:7, Marko 15:37-39, Aheb. 2:14-18, 3:1-4, 4:14-16, 5:1-6, 7:19-28 73 Ex. 28:1, 30:30 74 Aheb. 2:14-17, 3:1, 4:14-15, 5:5-10, 7:26-28, 9:11-28 75 Aro. 2:5-6, 5:18, 14:10-12, 11 Akor. 5:10, Aheb. 9:27, Yoda 6, 14-15 76 Marko 16:15, Luka 9:60-62, Mac. 10:42, Aro. 10:13-15, 1 Akor. 1:17-18, II Tim. 4:2 77 Chiv. 17:3-15, 18, 18:2-13, 23-24

Zaka 50 zapitazo Bishopu Wamkulu dzina lake Gilroy anati:

**"Chifukwa mapositi ofesi akuyendetsedwa ndi ife Akatolika, dipatimenti ya mtengatenga ndi mtokoma ili ndi njira zofufuzira kumene kuli anthu enaake omwe si a Roma Katolika [achikunja] momwe akuyendera ndi zina zimene zikuwachitikira. Ndipo pamene tili ndi anthu oterewa amene akuyendetsa zinthu m'mapositi ofesi athu ndikukugwilirani ntchito, tisade nkhwala ndi apolisi athu a chinsinsi kuti atigwira."**

Zimenezi, zikusonyezeratu chifukwa chimene dipatimenti ya mtengatenga ndi mtokoma panopa ikuyesetsa kuti ititsekereze kuti tisamatuminzeno makalata ambirimbi. Iwowa akuphera anthu ufulu wawo wolankhula zakukhosu ndiponso ufulu wopembedza, zitsimikizo ziwiri zomalizira zamalamulo aboma zimene Vatican mwachangu ndi mwabata akuyesetsa kuti achotse. Boma pamodzi ndi nthambi zake zonse, ndi nyumba zake zofalitsa nkhanu komanso makhoti m'dziko lililonse, pansi pa ulamuliro ochokera ku Roma, ndizachidziwikire linena kuti *Zinsinsi za Papa* ndi zolemba za "chindunji" ndipo akuuzani kuti ineyo ndine mdani wanu. Koma, monga Mtumwi Paulo ananenera, inenso ndikuti "Kotero kodi ndasadunda mdani wanu, pakukunenerani zoona?" (Agalatiya 4:16).

Ineyo ndikuua anthu zoona zenizeni, n'cholinga choti athawe m'gulu limene mtsogoleri wake ndi mtumiki wa Satana wankhanza kwambiri ndipo akuika malamulo opondereza ochokera ku Roma kuti dziko lathu la U.S. liziyendera m'malo mwa malamulo oyendetsera dziko lathuli (limene lili lamulo ku United States), ndicholina chakuti anthu a mitundu yonse athawe kuti asalandire Lemba la Chirombo komanso asadzapite ku Gehena—kodi mungati umene wo ndiudani? Yesu ananena kuti kuuza ena choonadi ndi chikondi ndipo anatilamula kuti tipite kumitundu yonse ya anthu kukalalikira choonadi,<sup>76</sup> pakuti Yesu anati, "**Mudzazindikira choonadi, ndipo choonadi chidzakumasulanu**" (Yohane 8:32).

Inuyo mukhonza kusankha kukhulupirira papa kapena kukhulupirira ine. Ndakuululirani inu zocheba chabe mwa zinsinsi zimene papa ali nazo. Mulungu anati bungwe la papa ndi chimake cha tchimo lililonse padzikolo lapansili, osati zoipa 99 pa 100 zili zonse, koma zoipa zonse.<sup>77</sup> Werengani Baibulo lanu Lopatulika la King James Version ndikuona ngati ndikukuuzani kapena sindikukuuzani zoona. Khulupirirani Mulungu.. "**Ukhulupirire pa Ambuye Yesu, ndipo udzapulumuka**" (Machitidwe 16:31).

*Ngati mukufuna kudziwa zambiri kapena ngati mukufuna mabuku kapenanso nkhanu zina zimene zimakusangalatsani, tiimbiren'i foni kapena tilembereni.*

**Tony Alamo, World Pastor, Tony Alamo Christian Ministries Worldwide • P.O. Box 2948, Hollywood, CA 90078**

**Twenty-four hour prayer and information line: (661) 252-5686 • Fax (661) 252-4362**

**www.alamoministries.com • info@alamoministries.com**

*Tony Alamo Christian Ministries Worldwide imalandira anthu onse ndipo imapereka zinthu zofunika Kwa onse amene ali ku U.S. amene akufunitsadi kuti ayambe kutumikira AMBUYE ndi mtima wawo wonse moyo wawo wonse ndi mphamvu zavo zonse*

**Maservice amachitikira ku New York City lachiwiri lililonse nthawi ya 8 koloko usiku ndi malo ena usiku okhaokha.**

**Chonde imbanu (908) 937-5723 kuti mudziwe zambiri. ZAKUDYA ZIMAGAWIDWA PAMAPETO PA MAPEMPHERO ALIWONSE.**

**Funsani buku la M'busa Alamo, lakuti Mesiya, losonyeza KHRISTU kuyambira ku Chipangano Chakale mu maulosi oposa 333.**

**Khalani wogwira ntchito yokolola miyoyo ya anthu pakukhala ogawira mabuku a M'busa Alamo**

**Mabuku ndi zinthu zonse zomvetsera n'zaulere, ndipo simulipira ndalamala yotumizira**

**Ngati wina akukuuzani kuti mupereke ndalamala pa zinthu zimenezi, chonde imbanu pa (661) 252-5686.**

**M'BUKU ILI MULI CHIKONZERO CHENICHENI CHA CHIPULUMUTSO (Machitidwe 4:12).**  
**MUSALITAYE, PATSANI ENA KUTI AWERENGUE.**

**Anthu amene muli m'mayiko ena, tikukulimbikitsani kuti mumasulire n'chinenero chanu mabukuwa. Ngati mukusindikizanso bukuli, musaiwale kuika mawu ali m'munsiwa omwe ndi okhudzana ndi zamalamulo:**

© Copyright 1983, 2006, 2012, 2013, 2014 All rights reserved World Pastor Tony Alamo \*Registered 1983, 2006, 2012, 2013, 2014

CHICHEWA/NYANJA—The Pope's Secrets